MFARISI WOTOLERA MSONKHO

...pakuti yense wakudzikuza adzachepetsedwa; ndipo amene adzichepetsa yekha adzakulitsidwa. LUKA 18:14

Ndimo nanena fanizo ili kwa ena omwe anadzidalira mwa iwo wokha kuti anali olungama, napeputsa ena: Amuna awiri anakwera ku tempile kukapempera; wina Mfarisi, ndi wina wamsonkho. Mfarisiyo anaimirira napemphera chotero mwa iye yekha, Mulungu, ndikukuyamikani kuti sindiri monga anthu ena, olanda, osalungama, achigololo, kapenanso monga wamsonkho uyu. Ndisala kudya kawiri pa sabata, ndipereka limodzi la magawo khumi la zonse ndiri nazo. Ndipo wamsonkhoyo adayimilira patali sanafuna ngakhale kukweza maso ake kumwamba, koma adadziguguda pachifuwa chake, nanena, Mulungu mundichitire chifundo, ine wochimwa. Ndinena ndi inu, Munthu uyu adatsikira kunyumba kwake woyesedwa wolungamayo koposa uja; pakuti yense wakudzikuza yekha adzachepetsedwa; ndipo amene adzichepetsa yekha adzakulitsidwa. LUKA 18:9-14

...Saiwala kulira kwa odzichepetsa. SALIMO 9:12

Yehova adzadula milomo yonse yosyasyalika, ndi lilime lolankhula zonyada: MASALIMO 12:3

Wodala munthu amene apanga Yehova cikhulupiriro cace, wosayang'ana odzikuza, kapena akupatukira kubodza. SALIMO 40:4

Ngakhale Yehova ali wokwezeka, ayang’ana wonyozeka; SALIMO 138:6

Pakudza kudzikuza padzanso manyazi; koma nzeru ili ndi odzichepetsa. Miyambo 11:2

Yehova adzawononga nyumba ya onyada, koma adzakhazikitsa malire a mkazi wamasiye. Miyambo 15:25

Kuopa Yehova ndiko mwambo wanzeru; ndipo patsogolo ulemu ndi kudzichepetsa. MIYAMBO 15:33

Yense wonyada mtima anyansidwa ndi Yehova; Miyambo 16:5

Kunyada kutsogolera chiwonongeko, ndipo mzimu wodzikuza kutsogolera kugwa. Kukhala wodzichepetsa ndi wonyozeka kuli bwino kuposa kugawana zofunkha ndi odzikuza. Miyambo 16:18-19

Chiwonongeko chisanadze mtima wa munthu udzikuza; ndi kutsogolera ulemu kudzichepetsa. Miyambo 18:12

Kudzichepetsa ndi kuopa Yehova ndiko chuma,
ndi ulemu, ndi moyo. MIYAMBO 22:4

Kunyada kwa munthu kudzamchepetsa;
koma wodzichepetsa mtima udzapeza ulemu.
Miyambo 29:23

Woipa pakudzikuza kwace azunza osauka; Pakuti woipa adzitamandira ndi zokhumba za mtima wake, Nadalitsa wosirira, amene Yehova anyansidwa naye. Woipa, mwa kudzikuza kwa nkhope yake, sadzafunafuna Mulungu; SALIMO 10:2-4

Pakuti akupanga iwe ndani kusiyana ndi wina? ndipo uli ndi chiyani kuti sudalandire? tsopano ngati unalandira, udzitama bwanji, monga ngati sunaulandira? 1 AKORINTO 4:7

Koma apatsa chisomo chochuluka. Chifukwa chake anena, Mulungu akaniza odzikuza, koma apatsa chisomo kwa odzichepetsa. YAKOBO 4:6

Momwemonso, anyamata inu, mverani akulu;
Inde, nonse inu mverana wina ndi mzake, ndi kuvala kudzichepetsa: pakuti Mulungu akaniza odzikuza, napatsa chisomo kwa odzichepetsa. Chifukwa chake dzichepetseni pansi pa dzanja lamphamvu la Mulungu, kuti pa nthawi yake akakukwezeni: 1 PETRO 5:5-6

Pakuti zonse za m’dziko lapansi, chilakolako cha thupi, chilakolako cha maso, matamandidwe a moyo, sizichokera kwa Atate, koma kudziko lapansi. 1 YOHANE 2:16